# Maphunziro a anyamata ndi atsikana a zaka 12-17


1. Colinga ca miyoyo yathu
2. Kuthetsa mabvuto
3. Ubwenzi
4. Kukakamizidwa ndi abwenzi
5. Kusamalira cilengedwe ndi thupi langa
6. Tsogolo langa

## Phunziro 1 Colinga ca miyoyo yathu

<u>Cofunikira pa nthawi yophunzitsa</u>
- Bolodi
- Coko
- Baibulo

## 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani onse.
- Fotokozani kuti anyamata ndi atsikana adzaphunzitsidwa mfundo zosiyana-siyana, mwacitsanzo ubwenzi, kudzisamalira ndi tsogolo lathu.
- M'phunziro lirilonse tidzawerenga Baibulo cifukwa maphunziro onse akhala cabe pa zimene Baibulo likamba.

<u>Zidziwitso</u>
- Maphunzirowa ndi a anyamata ndi atsikana a zaka 12-17.
- Phunziro lirilonse lidzayamba pa nthawi ya ………………. koloko. Onse afike pa nthawi yake cifukwa ngati acedwa sitidzakhala ndi nthawi yokwanira.
- Ndi cofunikira kwambiri kubwera ku maphunziro onse.
- Aphunzi ayenera kulowa ndi Baibulo m'maphunziro onse. Tidzalifuna pophunzira maphunziro a m'Baibulo.
- M'phunziro lotsiriza tidzalemba mayeso (mphunzitsi adzasankha ngati mayeso adzalembedwa). Kulemba mayeso sikudzakhala bvuto ngati mudzaphunzirako maphunziro onse.

<u>Malamulo</u>
- Ana a zaka zocepera 12 sadzaloledwa, ndiponso osabwera ndi ana ang'ono-ang'ono.
- Osayenda-yenda (pitani ku cimbudzi musanayambe kuphunzira).
- Khalani bwino ndipo mverani bwino mphunzitsi wanu. Khalani omasuka.

- Funsani ngati aphunzi ali ndi mafunso.
- Pemphani Mulungu dalitso la phunziro iri.

## 2. Kulengedwa (10 min)
- Funsani anyamata ndi atsikana kuti dziko lapansi licokera kuti: ciyambi cake cinali cotani? Auzeni kupereka mayankho osiyana-siyana omwe iwo anamva ku calichi, ku sukulu ndi m'mudzi. Lembani mayankho ao pa bolodi.
- Auzeni kuti tikhulupirira kuti Baibulo ndi coonadi. Baibulo litiuza kuti Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Kulenga kutanthauza kupanga cinthu kunalibe kanthu. Mulungu sanalengedwe koma analiko nthawi zonse.
- Auzeni kupereka zitsanzo za zolengedwa, mwacitsanzo mitengo, anthu, mbalame ndi mitambo.
- Auzeni kuti lero tidzaganizira ciyambi ca dziko lapansi. Ciyambico ciri ndi zotsatira kuli miyoyo yathu.

## 3. Genesis 1 ndi 2 (20 min)

- Funsani aphunzi kuti dziko lapansi labwino kwambiri lioneka lotani kulingana ndi iwo.
- Fotokozerani nthano ya kulengedwa kwa zonse (Genesis 1 ndi 2). Fotokozani zimene Mulungu analenga pa tsiku lirilonse. Fotokozani kuti zonse zinali zabwino kwambiri, cifukwa Mulungu yekha ndi wabwino ndi woyenerera.
- Fotokozani kuti kunali ubwenzi wabwino:
  A. Ubwenzi wa anthu ndi Mulungu: kunali cikondano, kunalibe cisokonezo. Mulungu ankalankhula ndi Adamu ndi Hava tsiku ndi tsiku. Ankayenderana nao. Adamu ndi Hava anadziwa Mulungu ndipo anamkonda.
  B. Ubwenzi wa anthu: kunali cikondano, kunalibe ndeu.
  C. Ubwenzi wa anthu ndi cilengedwe cina: zonse zinali m'ubwenzi wabwino, kunalibe mantha kapena imfa. Anthu sanadwale, nyama sizinali zoopsa.
- Fotokozani kuti zonse zinali zabwino kwambiri. Anthu anakhala kulingana ndi colinga ca Mulungu: anamumvera ndi kutumikira Mulungu. Anakhala nao moyo.

## 4. Kuwerenga Baibulo (30 min)

- Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao.
- Werengani pamodzi <u>Genesis 3.1-13</u> ndi <u>Genesis 3.22-24</u>.
- Lembani mafunso awa pa bolodi ndipo uzani aphunzi kuyankha mafunsowa m'magulu ang'ono.

### Mafunso

1. Fotokozani mwacidule zimene zinacitika kulingana ndi Genesis 3.
2. Ndi cifukwa ciani Adamu ndi Hava anadya zipatso zimene Mulungu anawaletsa kudya?
3. Atacimwa Adamu ndi Hava, ndi ciani cimene cinacitika ndi ubwenzi wa Mulungu ndi anthu?
4. Ndi ciani cimene cinacitika ndi ubwenzi pakati pa anthu?
5. Ndi ciani cimene cinacitika ndi ubwenzi wa anthu ndi zolengedwa zina zonse?
6. Taphunzira kuti zonse zinasinthika pamene Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu. Kodi Mulungu anasinthikanso?
7. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi kuli Satana?

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Fotokozani mwacidule zimene zinacitika kulingana ndi Genesis 3.**
     Yankho: Anthu sanamvere Mulungu. Anadya cipatso coletsedwa. Kusamvera ndi chimo. Kusamvera kwao kunali bvuto lalikulu pakuti zonse zinasinthika kucokera pa nthawi iyo.
  2. **Ndi cifukwa ciani Adamu ndi Hava anadya zipatso zimene Mulungu anawaletsa kudya?**
     Yankho: Anakhulupirira Satana amene adawauza kuti iwo adzakhala ngati Mulungu ndiponso kuti sadzafa atacitira Mulungu mwano.
  3. **Atacimwa Adamu ndi Hava, ndi ciani cimene cinacitika ndi ubwenzi wa Mulungu ndi anthu?**
     Yankho: Ubwenzi ndi woonongeka. Adamu ndi Hava anaopa pozindikira kuti acimwa. Mulungu anawacotsa m'munda wa Edeni. Ubwenzi unatha. Anthu ocimwa saloledwa kukhala pafupi ndi Mulungu. M'malo mwa ubwenzi kuli udani (kucimwa kutanthauza kuda Mulungu).

4. **Ndi ciani cimene cinacitika ndi ubwenzi pakati pa anthu?**
   Yankho: Ubwenzi ndi woonongeka. Kuli mabvuto ambiri pakati pa anthu, monga tiona tsiku ndi tsiku m'miyoyo yathu. Adamu ndi Hava atacimwa, anayamba kuikana mlandu.
5. **Ndi ciani cimene cinacitika ndi ubwenzi wa anthu ndi zolengedwa zina zonse?**
   Yankho: Ubwenzi unatha. Nyama zinayamba kubvutitsa anthu, nyama zina zimaopa anthu.
6. **Taphunzira kuti zonse zinasinthika pamene Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu. Kodi Mulungu anasinthikanso?**
   Yankho: Iai, Mulungu sanasinthike. Iye akhalabe Mulungu woyera ndi woyenerera monga anakhala pa ciyambi.
7. **Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi kuli Satana?**
   Yankho: Satana anali woyamba wonena bodza. Iye ndi wosakhulupirika. Afuna kutiononga. Koma sitiloledwa kuika mlandu pa Satana, cifukwa ife anthu asankha kumumvera cifukwa ca mtima wao woipa.

## 5. Nthano ya m'Baibulo (20 min)

- Masulirani bwino mogwiritsa nchito mau osabvuta, nthano yopezeka m' Genesis 3.1-13 ndi Genesis 3.22-24 (uphunzitsi wa Sukulu Sondo wa ana).
- Fotokozani kuti kucokera ku nthawi iyo, anthu alephera kukhala momwe Mulungu afuna. Anthu onse ndi ocimwa (mtengo wa mango ubereka mango cabe). Mtima wa anthu onse ndi wosinthika: m'malo mwa kudzipereka kwa Mulungu ticita zimene Mulungu aletsa, tiganiza kuti tidziwa bwino kuposa Mulungu.
- Funsani anyamata ndi atsikana zitsanzo za macimo ndipo lembani mayankho ao pa bolodi. Chimo litanthauza: kucita zoletsedwa ndi Mulungu komanso kusacita zimene Mulungu atilamulira.
- Afotokozereni kuti kulingana ndi Baibulo, Mulungu afuna kuti tizimtumikira ndi mtima wathu wonse, nzeru zathu zonse ndiponso macitidwe athu onse, nthawi zonse. Ngakhale kuganiza cinthu coletsedwa ndiko chimo: Mulungu adziwa zonse!
- Fotokozani kuti anthu ocimwa ayenera kulangidwa ku Gehena nthawi zonse cifukwa ca macimo ao. Fotokozani kuti kuli Njira imodzi cabe yopulumutsidwiramo: Yesu Kristu amene anafa pa mtanda cifukwa ca macimo. Aliyense amene akhulupirira Yesu (kuulula macimo ake ndi kudzipereka kwa Yesu) akhululukidwa ku macimo ake ndipo adzakhala ndi Mulungu Kumwamba muyayaya.

## 6. Colinga ca miyoyo yathu (10 min)

- Uzani anyamata ndi atsikana kukambirana za colinga ca miyoyo yao: Ndi cifukwa ciani ali pa dziko lapansi?
- Atakambirana, auzeni kupereka mayankho ao m'gulu lonse.
  Yankho: tiri pa dziko lapansi kumvera, kutumikira ndi kulemekeza Mulungu.
- Afunseni funso iri, 'Tingamumvere, tingamtumikire ndi kumlemekeza bwanji Mulungu?'
  Yankho: Ngati tidziwa ndi kucita zimene zilembedwa m'Baibulo.
- Fotokozani kuti m'maphunziro ena atsogolo, tidzaganiza za miyoyo yathu ndi zimene Mulungu akamba kuli miyoyo yathu. Akumbutseni kuti ndife olengedwa ndi Mulungu. Iye ndi Mwini wathu ndipo tiyenera kucita zimene Iye afuna!

## 7. Sewero (10 min)

- Mphunzi aliyense akhale pafupi ndi mnzake umodzi. Auzeni kusewera sewero iri:
  Mphunzi m'modzi achula cinthu cimodzi colengedwa ndi Mulungu (mwacitsanzo dzuwa). Mnzake ayenera kuchula cinthu cina cimene ciyamba ndi lembo lotsiriza la liu lokambidwa ndi mnzake (dzuw**a** – **a**mai). Mnzake ayenera kuchula liu lina loyambira ndi lembo lotsiriza la liu lokambidwa ndi mnzake, ndi zina zotere. Mwacitsanzo: dzuw**a** – **a**ma**i** – insw**a** - **a**nth**u** – **u**siku.

## 8. Kutsiriza (5 min)

- Funsani aphunzi zimene aphunzira lero.
- Bwezeraninso kuti colinga ca miyoyo yathu ndico kumtumikira, kumumvera ndi kumlemekeza Mulungu m'zonse zomwe ticita. Fotokozani kuti tiyenera kudziwa Yesu kuti timvere Mulungu moyenerera. Aphunzitseni 1 Akorinto 10.31b, 'Citani zonse ku ulemerero wa Mulungu'.
- Pempherani.

## Phunziro 2 Kuthetsa mabvuto

<u>Cofunikira pa nthawi yophunzitsa</u>
- Bolodi
- Coko
- Baibulo

## 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Funsani anyamata ndi atsikana zimene akumbukira za m'phunziro 1.

## 2. Kufotokoza (10 min)
- Fotokozani kuti kucokera pa nthawi ya kucimwira Mulungu (monga tinaphunzira m'phunziro 1), timakomana ndi mabvuto ambiri m'miyoyo yathu.
- Funsani aphunzi kuti akomana ndi mabvuto otani m'miyoyo yao. Ganizirani za mabvuto osiyanasiyana: kuli makolo/abwenzi, ku sukulu, zosowa m'umoyo ndi zina zotere.
- Fotokozani kuti pamene pali bvuto, tiyenera kusankha kucita ciani: kuyesa kulithetsa kapena kusayesa kulithetsa. Zonse zimene tingacite ziri ndi cotsatira cake: cithandiza kapena sicithandiza. Fotokozani kuti tiri ndi mphamvu kucita kanthu, ngakhale ndi kanthu kakang'ono. Ngati siticita kanthu, kulinso cotsatira!

## 3. Zolowapo (30 min)
- Kambiranani pamodzi zolowapo izi (kapena zilembeni pa bolodi ndi kuuza aphunzi kuyankha mafunso m'magulu ang'ono).

**Colowapo 1: Saulos**
Saulos ali ndi zaka 12. Amakhala ku Petauke. Mai wake anafa pamene Saulos anali ndi zaka 5. Tate wake anakwatira mkazi wina koma Saulos amvera kuti sasamalidwa bwino. Nthawi zina mkazi wa tate wake amuuza kuti ayenera kukhala ku nyumba ina. Akambirana kwambiri ndipo Saulos samvera bwino.
**Mafunso:**
1. **Ndi cifukwa ciani Saulos samvera bwino?**
   Yankho: Sakumva kuti makolo amkonda.
2. **Kulingana ndi inu, Saulos ayenera kucita ciani? Ndi cifukwa ciani ayenera kucita motere?**
   Yankho: Kupemphera, kupempha thandizo kwa munthu wanzeru kapena kufunsa wina a m'banja kuti angamlole kukhala nao.

**Colowapo 2: Marita**
Marita ali ndi zaka 14. Mnyamata wa ku sukulu anampatsa mimba. Marita adera nkhawa za tsogolo lake ndipo aopa kuuza munthu wina za mimba yake. Sakhoza kugona cifukwa sadziwa cimene adzacita. Marita apanikizika.
1. **Kambiranani pamodzi zimene Marita angacite. Patsani yankho zitatu zosiyana-siyana.**
   Yankho: Kuuza mnyamata, kufunsira upangiri kwa munthu wina, kupempha Mulungu kumpatsa nzeru ndi cikhululukiro.

2. **Ngati ndinu mnzake wa Marita, mumuuze kucita ciani kodi? Ndi cifukwa ciani mumuuze kucita tero?**
   Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha. Fotokozani kuti kutaya mimba si yankho kulingana ndi Baibulo.

**Colowapo 3: Luka**

Luka ali ndi zaka 17. Sanatsirize sukulu cifukwa kunalibe ndalama yolipira sukulu. Luka alibe nchito ndipo masiku onse sadziwa kucita cinthu cina ciriconse. Makolo ake afuna kuti apeza nchito koma Luka sakwaniritsa kuipeza. Ici cibvutitsa banja lonse. Luka afuna kuiwala bvuto lake ndipo ayamba kumwa mowa ndi kupepa fodya.

1. **Kodi kumwa mowa ndi kupepa fodya kuthandiza kuthetsa mabvuto m'njira yotani?**
   Yankho: Kuthandiza kuiwala cabe, koma sikuthetsa bvuto.
2. **Kodi kumwa mowa ndi kupepa fodya kuthetsa mabvuto? Ndi cifukwa ciani mwayankha motere?**
   Yankho: Iai, kumwa mowa ndi kupepa fodya sikuthetsa mabvuto. Koma mabvuto amacuruka cifukwa mufuna ndalama yogula mowa ndi fodya.
3. **Kodi ngati ndinu mnzake wa Luka, mumuuze kucita ciani? Ndi cifukwa ciani mwayankha motere?**
   Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

**Colowapo 4: Edina**

Edina ali ndi zaka 12. Ali m'giredi 5 ndipo amacita bwino ku sukulu. Koma mphunzitsi wake samcitira bwino. Pamene alakwa mphunzitsi wake amuuza kubwera kutsogolo ndipo ayamba kufotokoza kuti ndiye mwana wopusa amene sadzalemba bwino mayeso m'giredi 7. Edina samvera bwino ku sukulu ndipo aganiza za kuleka kupita ku sukulu.

1. **Ndi cifukwa ciani Edina apanikizika?**
   Yankho: Akumva kuti sacitidwa bwino, mphunzitsi wake samumvetsa ndipo akumva monga akhala cabe.
2. **Kodi ngati ndinu mnzake wa Edina, mumuuze kucita ciani?**
   Yankho: Mwacitsanzo kumthandiza, kumpangira, kupita naye kukauza munthu wina zimene ziri kucitika, kumcitira bwino.
3. **Kodi mudziwa anthu amene abvutidwa monga Edina?**
   Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

- Fotokozani kuti ng'anga si wanzeru kuti tingampemphe thandizo (Levitiko 19.31, Levitiko 20.27, Cibvumbulutso 22.15).

## 4. Kuwerenga Baibulo (20 min)

- Fotokozani kuti m'Baibulo tiwerenganso za anthu obvutika. Tidzawerenga nthano ya Bartimeyu ndi m'mene bvuto lake linacotsedwa.
- Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao.
- Werengani pamodzi Marko 10.46-52.
- Pang'ani magulu ang'ono ndipo uzani aphunzi kuyankha mafunso awa omwe mulemba pa bolodi.

**Mafunso**
1. Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m'nthano iyi.
2. Kodi kulingana ndi inu, Bartimeyu anamva bwanji pa kukhala wakhungu?
3. Kodi Bartimeyu anacita ciani kuti bvuto lake licotsedwe?
4. Ndi ciani cimene ciri cofunikira coposa pamene tikomana ndi mabvuto?
5. Anthu ena amene anali pafupi ndi Bartimeyu anafuna kuti aleke kupfuula kwa Yesu. Sanamthandize. Kodi mudziwa anthu amene akhoza kukuthandizani pamene muli ndi bvuto m'moyo wanu?

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m'nthano iyi.**
     Yankho: Bartimeyu anali wakhungu. Anapempha Yesu thandizo lake. Yesu anamciritsa.
  2. **Kodi kulingana ndi inu, Bartimeyu anamva bwanji pa kukhala wakhungu?**
     Yankho: Mwacitsanzo anakhala wacisoni, wosasamalidwa, wopanikizika.
  3. **Kodi Bartimeyu anacita ciani kuti bvuto lake licotsedwe?**
     Yankho: Anapempha Yesu kumthandiza.
  4. **Ndi ciani cimene ciri cofunikira coposa pamene tikomana ndi mabvuto?**
     Yankho: Kupempha Mulungu thandizo ndi nzeru kuti tidziwe kucita ciani.
  5. **Anthu ena amene anali pafupi ndi Bartimeyu anafuna kuti aleke kupfuula kwa Yesu. Sanamthandize. Kodi mudziwa anthu amene akhoza kukuthandizani pamene muli ndi bvuto m'moyo wanu?**
     Yankho: Mwacitsanzo membala a mpingo, mphunzitsi kapena munthu m'mudzi.

## 5. Nthano ya m'Baibulo (20 min)

- Masulirani bwino mogwiritsa nchito mau osabvuta, nthano yopezeka m' Marko 10.46-52 (uphunzitsi wa Sukulu Sondo wa ana).
- Fotokozani zimene tingaphunzire m'nthano iyi:
  1. Mulungu ndi wamphamvu zonse. Akhoza kuthetsa bvuto lina lirilonse. Mpempheni thandizo.
  2. Baibulo liphunzitsa kuti ndife akhungu m'uzimu (2 Petro 1.9, Cibvumbulutso 3.17). Ici citanthauza kuti ndife ocimwa ndiponso kuti sitikhoza kudziwa Mulungu pokhapo ngati Mulungu atiyeretsa ku macimo athu. Mulungu afuna kucita tero cifukwa ca Yesu amene anafa pa mtanda kukhululukira macimo. Mpempheni cikhululukiro.

## 6. Sewero (10 min)

- Pangani magulu anai. Uzani gulu lirilonse kukonzekera nthano ya pa wailesi m'mene afotokoza zimene tiyenera kucita ngati tikomana ndi bvuto .
- M'modzi wa gulu lirilonse afotokozere nkhani yao ya pa wailesi.

## 7. Kutsiriza (5 min)

- Funsani aphunzi zimene aphunzira lero.
- Bwezeraninso kuti colinga ca miyoyo yathu ndico kumtumikira, kumumvera ndi kumlemekeza Mulungu m'zonse zomwe ticita. Fotokozani kuti tiyenera kudziwa Yesu kuti timvere Mulungu moyenerera. Aphunzitseni 1 Akorinto 10.31b, 'Citani zonse ku ulemerero wa Mulungu'.
- Pempherani.

## Phunziro 3 Ubwenzi

<u>Cofunikira pa nthawi yophunzitsa</u>
- Bolodi
- Coko
- Baibulo

## 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani onse ndipo pempherani.
- Funsani anyamata ndi atsikana zimene akumbukira za phunziro 2.
- Fotokozani kuti tinaphunzira kuti Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Anatilenga ndipo analenganso anthu ena onse. Cifukwa ca uchimo umene unalowa dziko lapansi, ubwenzi wonse ndi woonongeka, ngakhale ubwenzi wa munthu ndi mnzake. Lero tidzaganizira za kukhala bwenzi wabwino.

## 2. Citanthauzo ca ubwenzi (20 min)
- Funsani anyamata ndi atsikana citanthauzo ca 'ubwenzi'.
- Lembani mau awa pa bolodi.

| | | |
|---|---|---|
| cikondi | kukhala wacoonadi | kusakhulupirika |
| thandizo | kumvetsetsa | kusagwirizana |
| cisamaliro | kukhulupirika | kutsutsidwa |
| kudekha | ulemu | mjedo |
| nsanje | citsanzo cabwino | |

- Uzani mphunzi m'modzi pa nthawi kubwera ku bolodi. Afunseni kuti azungulire mau amene alimbikitsa ubwenzi wabwino ndi kukweza mau amene aononga ubwenzi wabwino.
- Kambiranani pamodzi za mau amene alimbikitsa ubwenzi wabwino ndi amene aononga ubwenzi wabwino.

## 4. Colowapo (10 min)
- Khalani pansi m'magulu ang'ono ndipo kambiranani colowapo ici:
  Mnzanu wa pa mtima akhala bwenzi wa munthu wakumwa mowa. Nthawi zambiri mnzanu apita ku malo omwera mowa kuti amwe ndi mnzakeyo watsopano. Ku sukulu zotsatsira za mayeso ake zikhala zoipa koposa. Kodi muyenera kucita ciani pokhala mnzake wa pa mtima?
- Atakambirana m'magulu ang'ono, kambiranani pamodzi.
  Yankho: Kumcenjeza, kuuza anthu ena kuti pamodzi mungathandize mnzanu kuleka kumwa mowa. Koma khalani maso kuti inu nomwe simuyambanso kumwa mowa.

## 5. Nkhani ya Alani (15 min)
- Aphunzitsi awerengere aphunzi nthano ya 'Alani ndi tomato woola'. Mutawawerengera kambiranani pamodzi, 'Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi?'

# Nkhani

**Tomato woola**

Alani anali ndi abwenzi awiri oipa. Makolo a Alani anali kumuuza nkhani za m'Baibulo ndi kumuonetsa zitsanzo zabwino, cifukwa anali ndi nkhawa pakuona iye ali kuyenda ndi anyamata awiri omwe sanali ndi makhalidwe abwino. Atate ake anamuuza kuti safunika kukhala nao, koma Alani anaganiza kuti kukhala nao cinali cabwino ndi coseketsa. Anaganizanso kuti sicingabweretse coipa ciriconse.

Tsiku lina atate ake anati kwa iye: 'Alani, pita ku munda ndipo ukatyole tomato umodzi wabwino.' Alani anathamanga kupita ku munda ndipo anabwerera msanga ndi tomato wabwino. Atate ake anati, 'Uike m'dishi umo'. Ndipo anamulangiza m'dishi momwe munalibe kanthu. Alani anacita monga anauzidwa. Atate ake anatinso, 'Pita kukatyola tomato woola uwiri'. Ici cinadabwitsa Alani. Koma anapita napeza tomato woola uwiri ndipo anapita nao kwa atate ake. 'Uike pamodzi ndi wabwino', anatero atate ake. 'Koma atate, tomato woola udzaononga tomato wabwino', anati Alani. 'Cita monga ndakuuza, Alani', anatero atate ake. Alani anamvera ndipo atate ake anaika dishi kutali.

Patapita masiku awiri Alani ndi atate ake anapita kukaona tomato utatu uja m'dishi. Tomato unalimo. Alani anali wodabwa kuona kuti tomato wabwino tsopano unali woola kwakuti unali wofunika kuutaya cabe komabe ndiye cinthu comwe anali kuciyembekeza.

'Tamvera tsopano, Alani', anatero atate ake, 'Ici cidzakhala tero ngakhale kwa mnyamata yemwe amakhala ndi anyamata oipa. Monga tomato wabwino unakhala woola cifukwa unali pamodzi ndi woola, tero mnyamatayo adzaphunzira makhalidwe oipa cifukwa apezeka pamodzi ndi anyamata a makhalidwe oipa.'

Baibulo likamba kuti 'Mayanjano oipa aipsa makhalidwe okoma', (1 Akorinto 15.33). Ici citanthauza kukhala ndi abwenzi oipa kudzaononga macitidwe abwino. Baibulo limanenanso kuti, 'Mnzao wa opusa adzaphwetekedwa' (Miyambo 13.20). Tsono mnyamata yemwe adzapitiriza kukhala ndi abwenzi a makhalidwe oipa nayenso adzakhala woipa, ndipo pothera adzapita ku ciononGeko, monga tomato woola unafunika kuponyedwa kutali.

Lekani kuti Ambuye Mulungu akupatseni mtima watsopano kuti mukhale m'modzi wa anthu ake okonda kukhala pafupi naye.

## 6. Kuwerenga Baibulo (20 min)

- Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao.
- Werengani pamodzi Marko 2.1-12.
- Khalani m'magulu ang'ono ndipo uzani aphunzi kuyankha mafunso awa omwe mulemba pa bolodi.

| **Mafunso** |
|---|
| 1. Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m'nthano.<br>2. Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi pa nkhani ya ubwenzi?<br>3. Abwenzi anai anapita kwa Yesu ndi bwenzi wao amene anadwala manjenje. Nanga ife tingapereke bwanji abwenzi athu kwa Yesu?<br>4. Kodi inu mungakhale bwanji bwenzi wabwino kwa anthu ena? |

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m'nthano.**
     Yankho: Anzake a munthu wodwala manjenje anampereka kwa Yesu.
  2. **Kodi tingaphunzire ciani m'nthano iyi pa nkhani ya ubwenzi?**
     Yankho: Mwacitsanzo kuthandizana, kuperekana kwa Yesu.
  3. **Abwenzi anai anapita kwa Yesu ndi bwenzi wao amene anadwala manjenje. Nanga ife tingapereke bwanji abwenzi athu kwa Yesu?**
     Yankho: Mwacitsanzo mwa kuwapempherera, kuwauza za Yesu ndiponso kukhala citsanzo cabwino ca Mkristu wabwino.
  4. **Kodi inu mungakhale bwanji bwenzi wabwino kwa anthu ena?**
     Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

## 6. Nthano ya m'Baibulo (20 min)

- Masulirani bwino mogwiritsa nchito mau osabvuta, nthano yopezeka m' Marko 2.1-12 (uphunzitsi wa Sukulu Sondo wa ana).
- Fotokozani zimene tingaphunzire m'nthano iyi:
  1. Cikhululukiro ca macimo ndico cofunikira koposa.
  2. Abwenzi oona amathandizana kutumikira ndi kumvera Mulungu.

## 7. Sewero (10 minutes)

- Taphunzira kuti abwenzi amathandizana ndiponso kuti amakhulupirirana. Sewerani sewero kuonetsa izi ziwiri. Mangani mphunzi m'modzi ku maso. Mphunzi wina amuuza kumene ayenera kuyenda. Mphunzi m'modzi omangidwa maso ayenera kumvera bwino kwambiri ndi kukhulupirira kuti womthandiza athandiza bwino. Osagwirana, kambiranani cabe!

## 8. Kutsiriza (5 min)

- Funsani anyamata ndi atsikana zimene aphunzira lero.
- Bwezeraninso kuti colinga ca miyoyo yathu ndico kumtumikira, kumumvera ndi kumlemekeza Mulungu m'zonse zomwe ticita. Fotokozani kuti tiyenera kudziwa Yesu kuti timvere Mulungu moyenerera. Aphunzitseni 1 Akorinto 10.31b, 'Citani zonse ku ulemerero wa Mulungu'.
- Pempherani.

## Phunziro 4 Kukakamizidwa ndi abwenzi

Cofunikira pa nthawi yophunzitsa
- Bolodi
- Coko
- Baibulo

### 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Funsani anyamata ndi atsikana zimene akumbukira za phunziro 3.
- Bwezeraninso kuti kucokera ku nthawi ya kucimwa koyamba, zonse zionongeka. Ubwenzi wonse ndi woonongeka. Nthawi zina anthu abvutidwa ndi anthu ena kucita zimene iwo safuna kapena zimene siziri bwino. Ici ndi mutu wa lero: kukakamizidwa ndi abwenzi.

### 2. Kusewera sewero (10 minutes)
- Sankhani anyamata awiri ndi atsikana awiri kupita pabwalo.
- Fotokozani zocita kwa ena onse amene ali m'kati koma iwo amene akhala pabwalo asakumvereni.
- Fotokozani iwo amene akhala m'kati: ayenera kusewera sewero monga ali kuyenda pa mseu ndipo akoma ndi anzao. Iwo onse amene akhala m'kati ndiwo anzao, koma amene akhala pabwalo si ndiwo anzao (koma okhala pabwalo sayenera kudziwa ici). Anyamata ndi atsikana amene akhala m'kati ayenera kusasamalira anyamata ndi atsikana amene akhala pabwalo. Ngati iwo okhala pabwalo ayamba kulankhula, iwo okhala m'kati sawamvere ndipo sakambe nao. Ngati afuna kupatsa moni, iwo ayenera kuwakanira.
- Itani iwo amene akhala pabwalo kuti abwere m'kati ndipo fotokozani kwa onse kucita monga akuyenda pa mseu ndipo akumana ndi abwenzi ao.
- Sewerani sewero. Iwo amene anakhala pabwalo adzamvera kusasamalidwa cifukwa kulibe munthu aliyense amene afuna kukamba nao.
- Atasewera sewero, funsani iwo amene anakhala pabwalo kuti amvera bwanji.

### 3. Kukakamizidwa ndi abwenzi (5 minutes)
- Fotokozani citanthauzo ca 'kukakamizidwa ndi abwenzi'. Citanthauza: kukakamizidwa kucita zimene abwenzi ndi ena acita. Ngati simucita zimene ena acita, simulandiridwa m'gulu. Simudzasamalidwa (cimodzimodzi monga iwo amene anakhala pabwalo pa nthawi ya sewero). Mau ena a 'kukakamizidwa ndi ubwenzi' ndi 'kukopedwa ndi gulu'.
  Mwacitsanzo:
  - Pamene muli kuceza ndi anzanu ndipo iwo onse ayamba kukoka fodya, mudzapanikizika kukokanso fodya. Ngati mukana, mudzamva monga inu si m'modzi wa gulu.
  - Pamene muona kuti anzanu onse anagula nsapato zatsopano, mudzafunanso nsapatso zatsopano.
  - Pamene gulu la anzanu afuna kuba, adzakukakamizani kuyenda nao.
- Uzani anyamata ndi atsikana kupatsa zitsanzo zina za kukakamizidwa ndi abwenzi.

## 4. Kuwerenga Baibulo (30 min)

- Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao.
- Werengani pamodzi nthano ya Sadrake, Mesake ndi Abedinego (Danieli 3).
- Atawerenga pamodzi, aphunzi akhale m'magulu ang'ono kuyankha mafunso awa omwe mulemba pa bolodi:

| **Mafunso** |
|---|
| 1. Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m'nthano. |
| 2. Ndi cifukwa ciani Sadrake, Mesake ndi Abedinego sanagwadire? |
| 3. Kodi tingaone bwanji citsanzo ca kukakamizidwa m'nthano iyi? |
| 4. Kodi tingaphunziremo ciani m'nthano iyi pa nkhani ya kukakamizidwa? |

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Fotokozani mwacidule zimene zinacitika m'nthano.**
     Yankho: Mfumu Nebukadinezara anafuna anthu onse kugwadira fano la golidi. Iwo amene sagwada adzaponyedwa m'ng'anjo ya moto. Anthu onse anagwada kupatula Sadrake, Mesake ndi Abedinego. Iwo anaponyedwa m'ng'anjo ya moto koma Mulungu anawapulumutsa.
  2. **Ndi cifukwa ciani Sadrake, Mesake ndi Abedinego sanagwadire?**
     Yankho: Mulungu atiletsa kugwadira ciriconse koma Iye yekha. Ndiye kugwadira fano la mfumu ndiko chimo.
  3. **Kodi tingaone bwanji citsanzo ca kukakamizidwa m'nthano iyi?**
     Yankho: Sadrake, Mesake ndi Abedinego anali anthu okha amene sanagwade. Anthu anawakakamiza kugwada. Kupanikizidwa kusamvera Mulungu kunali kwakukulu.
  4. **Kodi tingaphunziremo ciani m'nthano iyi pa nkhani ya kukakamizidwa?**
     Yankho: Imani nji, osalondola gulu, koma mverani Mulungu nthawi zonse. Mulungu akuonani ndipo akhoza kukupulumutsani (koma angakhale sakupulumutsani, mverani Mulungu! Danieli 3.18).

## 5. Nthano ya m'Baibulo (20 min)

- Masulirani bwino mogwiritsa nchito mau osabvuta, nthano yopezeka m'Danieli 3 (uphunzitsi wa Sukulu Sondo wa ana).
- Fotokozani zimene tingaphunzire m'nthano iyi:
  1. Tiyenera kuima nji ndi kukana kucimwa.
  2. Mulungu ndi wamphamvu zonse.

## 6. Kufotokoza 'kukakamizidwa ndi abwenzi m'njira yabwino' (20 minutes)

- Fotokozani kuti lero tamva kuti kukakamizidwa ndi abwenzi ndi cinthu coipa. Koma kukakamizidwa ndi abwenzi kungakhale kwabwino m'njira ina. Kukakamizidwa ndi abwenzi m'njira yabwino kutanthauza: kulimbikitsidwa kwabwino ndi kupangiridwa bwino ndi abwenzi. Mwacitsanzo: Mnyamata m'mudzi sankapita ku calichi koma nthawi ina anapitako cifukwa anzake onse anapita.
- Citsanzo cina ca kukakamizidwa ndi ubwenzi m'njira yabwino ndi ici:
  Rakele (12) ndi Davide (14) anali ana a masiye pamene amai ao anafa zaka ziwiri zapitazo. Amakhala ku nyumba ya agogo ao, koma agogo ao ndi okalamba ndi ofooka kwambiri. Sabata latha Rakele ndi Davide anayamba kuphunzira ku sukulu lanu. Amaoneka ngati akumva cisoni. Kodi anzao ao angacite ciani kuti iwo akhale omasuka koposa?
- Kambiranani pamodzi za izi.

## 7. Closing (5 min)

- Funsani anyamata ndi atsikana zimene aphunzira lero.
- Bwezeraninso kuti colinga ca miyoyo yathu ndico kumtumikira, kumumvera ndi kumlemekeza Mulungu m'zonse zomwe ticita. Fotokozani kuti tiyenera kudziwa Yesu kuti timvere Mulungu moyenerera. Aphunzitseni 1 Akorinto 10.31b, 'Citani zonse ku ulemerero wa Mulungu'.
- Pempherani.

## Phunziro 5 Kusamalira cilengedwe ndi thupi langa

<u>Cofunikira pa nthawi yophunzitsa</u>
- Bolodi
- Coko
- Baibulo

## 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani onse.
- Funsani anyamata ndi atsikana zimene akumbukira za phunziro 4.
- Fotokozani kuti tinaphunzira kuti anthu onse analengedwa ndi Mulungu. Mulungu analenganso cilengedwe cina. Tidzaganizirako ici lero.

## 2. Kusamalira thupi langa (20 min)
- Fotokozani kuti Mulungu anatilenga. Cifukwa cace tiyenera kukhala maso ndi matupi athu ndi kuwasamalira bwino: makhalidwe abwino ndi ukhondo. Kodi tingamve bwanji ngati munthu wina sasamalira mphatso imene tinampatsa?
- Funsani anyamata ndi atsikana zitsanzo za m'mene tingasamalire matupi athu.
- Fotokozani *mwacidule* kuti kusamalira matupi athu kutanthauza:
  - Kudya ndi kumwa (osati zambiri, osati zazing'ono, cakudya cabwino ndi cakudya ca mtundu wosiyana-siyana)
  - Kusamalira bwino thupi kuti likhale labwino (kusamba, kutsuka mano, kusamba manja kutapita ku cimbudzi, ndi zina zotere) ndiponso kupita ku cipatala tikadwala.
  - Masewero olimbitsa thupi (masewero abwino athandiza thupi kukhala lolimba)
  - Kupumula ndi kugona (kugona bwino kuthandiza kucita bwino ku sukulu)
- Funsani anyamata ndi atsikana kuti cotsatira ca mowa ndi mankhawala ozunguza bongo ndico ciani kuli matupi athu.
  Yankho: Pa kumwa mowa ndi kugwiritsa nchito mankhwala ozunguza bonga, tiononga matupi athu. Kanani ndipo imani nji! (onani pa mfundo 3 za njira ya kukana).
- Funsani aphunzi kuti cotsatira ca dama ndi cigololo ndico ciani kuli matupi athu.
  Yankho: Ngati ticita izi, tiononga matupi athu. Mulungu satilola kusewera kotero ndi matupi athu. Kuli mpata waukulu wotenga matenda (STI's, HIV/AIDS) ndipo makhalidwe otero owawitsa m'mtima.

## 3. Cilankhulo ca m'thupi (20 min)
- Fotokozani kuti Mulungu anatipatsa matupi athu ndipo kuti tingawagwiritse nchito polankhula, mwacitsanzo maonekedwe a nkhope, kuyang'ana maso, kugwiritsa nchito manja/mapazi, kaimidwe ka thupi, mau (pamwamba/pansi, msanga/pang'ono).
- Uzani mphunzi m'modzi kupita pabwalo. Muuzeni kuti ayenera kupita patsogolo pa gulu ndi kuonetsa kuti ndiye wosangalala. Koma saloledwa kulankhula. Ndiye ayenera kugwiritsa nchito thupi lake kuonetsa kuti akumva bwanji. Aphunzi ena ayenera kuganizira kuti akumva bwanji.
  Uzani enanso kuonetsa: mantha, cisoni, manyazi.
- Fotokozani kuti cilankhulo ca m'thupi liyenera kugwirizana ndi mau pa nthawi yokambira.
- Fotokozani njira yogwiritsa nchito thupi pa kunena 'iai'. Patsani citsanzo ca kunena 'iai' mwamphamvu (molimba mau, kuyang'ana maso) ndi mofooka (kuyang'ana pansi,

kusalimba mau, kucita manyazi). Ngati tifuna kunena 'iai' mwamphamvu tiyenera kudziwa cifukwa cace ca kukana: ngati sitikhala otsimikiza za kukana, tidzakana mokayika. Ndiye dziwani zimene mufuna ndi zimene musafuna, ganizirani moyo wanu!

## 4. Kusamalira cilengedwe (20 min)

- Fotokozani kuti Mulungu sanalenge matupi athu ndi anthu ena cabe, komanso cilengedwe cina. Cifukwa cace tiyenera kucisamalira bwino, ticifuna kuti tikhale ndi moyo wabwino.
- Funsani anyamata ndi atsikana kupatsa zitsanzo za kusamalira bwino cilengedwe cotizungulira.
- Fotokozani kuti kusamalira cilengedwe kutanthauzanso:
  - Kutsuka (nyumba, cimbudzi, malo ozungulira nyumba).
  - Kutaya bwino zinyalala. Kutaya zinyalala m'cilengedwe cinyengerera kanyama kang'ono kamene kanyamula matenda. Kuononganso zomera ndi mitengo zimene tifunika kukhala ndi umoyo wathanzi.
    Potaya-taya zinyalala tiononga cilengedwe: nyama ndi tizirombo zingafe koma tizifuna cifukwa ca zipatso ndi masamba. Ng'ombe ndi nkhuku zimadya zomera, ndiye ngati cilengedwe ciri bwino, nyamanso zidzakhala bwino ndipo cakudya cathu zidzakhalanso bwino. Mphepo icokera m'mitengo ndi zomera. Anthu amakamba za kusinthika kwa nyengo: nthawi zambiri sitisamalira cilengedwe koma ticifunika!
    Kambiranani zimene tingacite ndi zinyalala zathu.
  - Kugwiritsanso nchito. Gwiritsaninso nchito zikwama, pangani zinthu zatsopano mogwiritsa nchito zinthu zakale, osangotaya zimene sitifunabe koma pezani njira yozigwiritsanso nchito kapena zitayeni bwino (onani pa 'kutaya zinyalala').
- Fotokozani kuti tiri ndi mphamvu yosintha cilengedwe cotizungulira ndi tsogolo lathu (phunziro 6).

## 5. Kuwerenga Baibulo (20 min)

- Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao.
- Werengani pamodzi Miyambo 12.10 ndipo yankhani pamodzi mafunso awa:
  1. **Kodi tingaphunzire ciani m'ndime iyi?**
     Yankho: Tingazindikire ngati tikonda Mulungu poona m'mene tisamalira nyama.
  2. **Kodi tiyenera kucita ciani kulinanga ndi ndime iyi? Patsani zitsanzo zitatu.**
     Yankho: Zitsanso zoonetsa kuti tiyenera kusamalira nyama. Sitiloledwa kuzipha koma cabe ngati ndizo zoopsa kapena ngati tizifuna kudya. Samalirani ng'ombe: osazimenya koposa. Kodi Mulungu akumva bwanji ngati mungocotsa mwendo wa cirombo pa cabe?

- Werengani pamodzi Genesis 2.15 ndipo yankhani pamodzi funso iri:
  3. **Tawerenga kuti Mulungu anafuna anthu kuzisamalira dziko lapansi. Patsani zitsanzo zitatu za njira zimene tingasamalire dziko lapansi m'miyoyo yathu.**
     Yankho: Aphunzi apatse zitsanso zosiyana-siyana.

- Werengani pamodzi Yohane 6.11 and 12 ndipo yankhani pamodzi funso iri:
  4. **Yesu ananena kuti cakudya sicitayike. Kodi mumataya cakudya? Ngati mumataya, mungacite ciani m'malo mwa kutaya?**
     Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.

## 6. Kutsiriza (5 min)

- Funsani anyamata ndi atsikana zimene aphunzira lero.
- Bwezeraninso kuti colinga ca miyoyo yathu ndico kumtumikira, kumumvera ndi kumlemekeza Mulungu m'zonse zomwe ticita. Fotokozani kuti tiyenera kudziwa Yesu kuti timvere Mulungu moyenerera. Aphunzitseni 1 Akorinto 10.31b, 'Citani zonse ku ulemerero wa Mulungu'.
- Pempherani.

## Phunziro 6 Tsogolo langa

<u>Cofunikira pa nthawi yophunzitsa</u>
- Bolodi
- Coko
- Baibulo

## 1. Kulandiridwa (10 min)
- Landirani onse ndipo pempherani.
- Funsani anyamata ndi atsikana zimene zinaphunzitsidwa m'phunziro 5.
- Fotokozani kuti tinaphunzira zambiri za kulengedwa kwa dziko ndi za macimo. Tinaphunzira kuti zonse ndi zoonongeka ndipo ziyenera kukonzedwanso mwa Yesu. Lero tidzaganizira m'mene tingatenge ulamuliro pa tsogolo lathu ndiponso za kukhala m'mene Mulungu atifuna kukhala. Tidzaganizira mfundo zosiyana-siyana za tsogolo lathu.

## 2. Zilakolako zathu (5 min)
- Uzani mphunzi aliyense kuuza mnzake za zolakolako zake za tsogolo. Kambani za: sukulu, ukwati, mudzi, nchito, umoyo wa masiku onse ndi zina zotere.
- Fotokozani kuti ife tonse tiri ndi maganizo a tsogolo lathu. Sitidziwa zimene zidzacitika m'tsogolo (Mulungu alamulira miyoyo yathu, Yakobo 4.15) komabe kuganizira tsogolo ndi kwabwino.

## 3. Sukulu (25 min)
- Funsani aphunzi ndi cifukwa ciani kupita ku sukulu ndi kofunikira.
- Fotokozani kuti kuli mabvuto ambiri otiletsa kupita ku sukulu kapena kutsiriza sukulu.
- Pangani magulu anai ndipo uzani gulu lirilonse kukambirana colowapo cimodzi. Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho.

**Colowapo 1 Belita**
Belita ali ndi zaka 14. Ali m'giredi 7. Aphunzitsi ake acimuna afuna kuyenda naye ca mwanseri. Mphunzitsi ali naye m'cikondi. Amamupatsa Belita ndalama, zobvala ndi sopo.
**Funso: Kodi ngati ndinu mnzake wa Belita, mudzamuuza kuti acite ciani?**
Yankho: Ayenera kusalandira mphatso, cifukwa ngati alandira, mphunzitsi adzaganiza kuti Belita amukonda ndipo ici cidzabweretsa mabvuto. Belita ayenera kuuza wina amene akhoza kumpangira bwino ndi kumthandiza kuima nji.

**Colowapo 2 David**
David ali ndi zaka 16. Ali m'giledi 9. Ali wocenjera kwambiri. Kulipira ndalama ya sukulu ndi kobvuta, koma akwaniritsa. Tsiku lina mnzake anena ndi iye: 'Bwera, tipite pamodzi, ndapeza njira kukhala wolemera. Udzapeza ndalama zambiri pogwira nchito zaka zocepa ndipo pambuyo pace udzapitiriza sukulu'.
**Funso: Kodi ngati ndinu mnzake wa Davide, mudzamuuza kuti acite ciani?**
Yankho: Davide ayenera kupitiriza sukulu monga anacita kale. Ngati aleka kupita ku sukulu, kuyambanso kudzakhala kobvuta. Cabwino coposa ndi kutsiriza sukulu kuti kenaka angagwiritse nchito. Komanso nchito yotero yopeza ndalama mwasanga ndiyo nchito yotani, kodi lamulo libvomereza nchito yotero?

**Colowapo 3: Gire**
Gire ali ndi zaka 17. Ali m'giledi 9. Asanalembe mayeso azindikira kuti ali ndi mimba. Adziwa dzina la mnyamata amene anampatsa cabe. Aganiza za kuleka sukulu ndi kusamalira mwana wake.
**Funso: Kodi ngati ndinu mnzake wa Gire, mudzamuuza kuti acite ciani?**
Yankho: Kupitiriza sukulu, kupeza wina amene angasamalire mwana ndiponso kuleka kusewera ndi anyamata.

**Colowapo 4: Benson**
Benson ali ndi zaka 15. Ali m'giredi 8. Makolo ake sakwaniritsa kulipira ndalama ya ku sukulu. Benson aganiza za kuleka sukulu ndi kupeza nchito.
**Funso: Kodi ngati ndinu mnzake wa Davide, mudzamuuza kuti acite ciani?**
Yankho: Kusaleka sukulu koma kupeza njira yogwira nchito kuti angathandize kulipira sukulu (mwacitsanzo maganyu). Ngati sakwaniritsa, ayenera kupita ku mphunzitsi wake kulankhula naye.

- Funsani anyamata ndi atsikana kupereka zitsanso zina za mabvuto owaletsa kupita ku sukulu ndiponso m'mene angathetse mabvutowa.
- Uzani aphunzi kukhala cidwi ku sukulu, cifukwa mwa kucita tero akonzekera tsogolo lao! Ngati akomana ndi mabvuto, ayenera kuuza wina amene angathandize kupeza yankho.
- Afunseni ngati adziwa anthu amene anatsiriza sukulu ndipo ali pa nchito tsono. Kodi anthuwo anakwaniritsa bwanji kutsiriza sukulu?

## 4. Nthenda ya kalionde-onde (HIV/AIDS) (15 min)

- Fotokozani kuti <u>anthu ena aganiza</u> kuti munthu wodwala HIV/AIDS alibe tsogolo labwino. Afotokozeni zoyambitsa za HIV/AIDS, mwacitsanzo kugonana kapena amai angapatse mwana wake asanabadwe.
- Muwawerengere ziganizo zolembedwa munsi. Ngati anyamata ndi atsikana aganiza kuti ciganizo ndi coona, ayenera kukweza dzanja. Ngati aganiza kuti ciganizo ndi cabodza, sayenera kukweza manja. Fotokozani kuti onse ayenera kuyankha pa iwo okha.
  1. **Ndi kotheka kuti anthu agwidwa ndi nthenda yakalionde-onde (HIV) koma sazindikira kuti ndiwo odwala ndipo aoneka kukhala ndi thanzi.**
     Yankho: Zoona.
  2. **Anyamata ndi atsikana anamwali sakhoza kupangitsa wina kukhala ndi nthenda yakalionde-onde (HIV/AIDS).**
     Yankho: Zabodza.
  3. **Ngati usamba utagona ndi mwamuna/mkazi, ungacotse nthenda yakalionde-onde (HIV).**
     Yankho: Zabodza. HIV/AIDS ndi nthenda ya m'mwazi.
  4. **Ngati munthu agona ndi anthu ambiri, ali ndi mphata waukulu wotenga matenda akalionde-onde (HIV/AIDS).**
     Yankho: Zoona.
  5. **Ngati mkazi amene akhala ndi nthenda yakalionde-onde (HIV-positive) abereka mwana, kuli mphata waukulu kuti mwana akhalanso ndi nthenda yakalionde-onde**
     Yankho: Zoona.

6. **Mwamuna angaciritsidwe ku matenda akatengera ngati agonana ndi mtsikana amene sanagonepo ndi mwamuna.**
   Yankho: Zabodza.
7. **Ngati ndiwe wodwala nthenda yakalionde-onde (HIV/AIDS) uyenera kuuza wokondedwa wako za kudwala kwako.**
   Yankho: Zoona.
8. **Ungatenge nthenda yakalionde-onde (HIV) pa kusamba ndi kumwa madzi ocokera pa citsime.**
   Yankho: Zabodza.
9. **Nthenda yakalionde-onde (HIV/AIDS) ibvutitsa anthu a ku Afirika cabe.**
   Yankho: Zabodza.
10. **Ena anatenga nthenda yakalionde-onde (HIV) ngakhale anagwiritsa nchito kondomu.**
    Yankho: Zoona.
11. **Anthu amene adwala nthenda yakalionde-onde (HIV/AIDS) angakhale moyo zaka zambiri ngati amamwa mankhwala ndi kumadya zakudya zabwino monga zipatso ndi zakudya zomanga thupi.**
    Yankho: Zoona.
12. **Kukhala wodwala nthenda yakalionde-onde (HIV/AIDS) kutanthauza kuti Mulungu samakukonda.**
    Yankho: Zabodza.
13. **Ngati anthu sacita cigololo ndi dama, bvuto la nthenda yakalionde-onde (HIV/AIDS) lingacepetsedwe.**
    Yankho: Zoona.

- Mangirirani kukambirana ndi kunena kuti tiyenera kukhala monga za m'Baibulo osagona ndi anthu osiyana-siyana.

## 4. Ukwati (15 min)
- Funsani anyamata ndi atsikana ngati adziwa anthu amene ali m'ukwati wabwino. Ndi ciani cimene cipangitsa ukwati wao kukhala wabwino? Lembani mayankho ao pa bolodi.
- Fotokozani kuti m'ukwati wabwino muli: kukhulupiririrana, kuperekana ulemu, kusamalirana. Khalani mwamuna/mkazi wabwino monga Mulungu afuna.
- Uzani aphunzi kukhala maso kuli ukwati, 'Kodi mufuna ukwati wotani?' Osathamangira ukwati: poyamba muyenera kudziwa konse mtsikana/mnyamata.

## 5. Kuwerenga Baibulo (15 min)
- Uzani aphunzi kutsegula Baibulo lao.
- Werengani pamodzi Yakobo 4.13-17.
- Pangani magulu ang'ono ndipo uzani aphunzi kuyankha mafunso awa omwe mulemba pa bolodi.

| **Mafunso** |
|---|
| 1. Kodi Yakobo alankhula za anthu otani m'ndime ya 13? |
| 2. Kodi mudziwa anthu amene amacita motere? |
| 3. Kodi Yakobo atanthauza ciani ndi 'muli utsi, wakuonekera kanthawi, ndi pamenepo ukanganuka' m'ndime ya 14? |
| 4. Ndi cifukwa ciani tiyenera kunena (ndi kuganiza) zimene zalembedwa m'ndime ya 15? |
| 5. Kodi ndime ya 17 itanthauzanji? |

- Itakomana 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:
  1. **Kodi Yakobo alankhula za anthu otani m'ndime ya 13?**
     Yankho: Analankhula za anthu amene odzikweza pa zimene akwaniritsa ndiponso za anthu oganizira za tsogolo lao monga kulibe Mulungu.
  2. **Kodi mudziwa anthu amene amacita motere?**
     Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.
  3. **Kodi Yakobo atanthauza ciani ndi 'muli utsi, wakuonekera kanthawi, ndi pamenepo ukanganuka' m'ndime ya 14?**
     Yankho: Ndife ofooka ndi osatetezedwa. Nthawi iriyonse tingafe. Tiyenera kukhala okonzeka mwa Yesu.
  4. **Ndi cifukwa ciani tiyenera kunena (ndi kuganiza) zimene zalembedwa m'ndime ya 15?**
     Yankho: Cifukwa tiribe mphamvu ya miyoyo yathu koma Mulungu atilamulira.
  5. **Kodi ndime ya 17 itanthauzanji?**
     Yankho: Tiyenera kucita zabwino osati kucimwa. Tinaphunzira zambiri m'maphunziro ndipo tiyenera kuzicita. Ngati sitizicita, tacimwa.

## 6. Mayeso (30 minutes)

*Mayeso awa si okakamiza. Mphunzitsi asankhe ngati aphunzi adzalemba mayeso kapena iai. Ngati adzalemba mayeso mphunzi aliyense afunika colembera ndi pepala.*

- Lembani mafunso opezeka pa pepala lotsiriza m'bukuli pa bolodi ndipo aphunzi alembe mayankho ao pa pepala lao (asankhe yankho A, B kapena C). Kapena: jambulani mayeso ndipo patsani mphunzi aliyense pepala limodzi.
- Atalemba mayeso aphunzi ayenera kupatsa mapepala ao kwa mphunzitsi.
- Mphunzitsi akonze zolakwika ndipo aconge mayeso. Mayankho abwino ali conco:

| | |
|---|---|
| 1. A | 6. B |
| 2. B | 7. B |
| 3. A | 8. C |
| 4. C | 9. B |
| 5. C | 10. - |

## 7. Kutsiriza (5 min)

- Funsani aphunzi zimene aphunzira. Alimbikitseni kuzicita.
- Bwezeraninso kuti colinga ca miyoyo yathu ndico kumtumikira, kumumvera ndi kumlemekeza Mulungu m'zonse zomwe ticita. Fotokozani kuti tiyenera kudziwa Yesu kuti timvere Mulungu moyenerera. Aphunzitseni 1 Akorinto 10.31b, 'Citani zonse ku ulemerero wa Mulungu'.
- Pempherani.

# Mayeso

Dzina ....................................................

1. Pa ciyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Ndi ciani cimene ciri coona?
   A. Kunali ubwenzi wabwino pakati pa Mulungu, anthu ndi cilengedwe.
   B. Mulungu sanalenge mitengo.
   C. Mulungu anatsiriza kulenga patapita masiku anai (4).

2. Kodi colinga ca miyoyo yathu ndico ciani?
   A. Kukhala anthu abwino.
   B. Kumvera, kumtumikira ndi kulemekeza Mulungu.
   C. Kumvera makolo athu.

3. Ndi cifukwa ciani tikomana ndi mabvuto m'miyoyo yathu?
   A. Cifukwa ca macimo.
   B. Cifukwa sitidziwa kuthetsa mabvuto.
   C. Cifukwa makolo athu anakalipitsa mizimu.

4. Kodi tiyenera kucita ciani pamene tikomana ndi mabvuto?
   A. Sitiyenera kucita kalikonse.
   B. Tiyenera kupita ku ng'anga kuti atilangize.
   C. Tiyenera kupempha Mulungu nzeru kuti tipeze mayankho abwino pa mabvuto athu.

5. Kodi ndi liu liti limene ligwirizana ndi ubwenzi?
   A. Kusakhulupirika.
   B. Citsanzo coipa.
   C. Thandizo.

6. Tinamva nthano ya m'Baibulo ya wodwala manjenje. Kodi anzake a munthuyo anacita ciani?
   A. Anamuiwala.
   B. Anamthandiza mwa kumpereka kwa Yesu.
   C. Analankhula zoipa za iye.

7. Kodi tiyenera kucita ciani pamene anthu ena atikakamiza kucimwa?
   A. Tiyenera kucita zimene afuna.
   B. Tiyenera kuima nji ndi kumvera Mulungu.
   C. Sitiyenera kucita ciriconse.

8. Ndi cifukwa ciani tiyenera kusamalira bwino matupi athu?
   A. Cifukwa tingacimwe ndi matupi athu.
   B. Cifukwa tifunika matupi a thanzi kuti tigwire nchito kukapeza ndalama.
   C. Cifukwa matupi athu ndiwo mphatso zocokera kwa Mulungu.

9. Ndi ciani cimene ciri cofunikira kwambiri m'ukwati?
   A. Mkazi amene amvera mwamuna wake nthawi zonse.
   B. Kukhulupirirana, ulemu ndi kusamalirana.
   C. Nyumba yabwino.

10. Lembani fundo ziwiri zimene mukumbukira bwino za maphunziro amene munaphunzira.

    1. ……………………………………………………………………………………………………………………………

       ……………………………………………………………………………………………………………………………

    2. ……………………………………………………………………………………………………………………………

       ……………………………………………………………………………………………………………………………